ZITHU ZOFUNIKA ZOMWE TAKHAZIKIKAMO

MKHRISTU

CHIYERO

WOTUMIDWA

Christian Holiness Missional

Chichewa

First Printing – 1000 – July 2004

ISBN 0-7977- 0673-9

Translated and printed with permission by

Africa Nazarene Publications
P.O. Box 1288
Florida
1710
Republic of South Africa

Chikhulupiliro Cha Moyo:
Zomwe Anazarene Amakhulupilira

Bungwe lina lililonse limene lakhala nthawi yaitali likugwira ntchito zake molimbika, limakhoza kukhazikitsidwa kuti lidzigwirira ntchito pamodzi ndi mabungwe ena, pofuna kukwaniritsa cholinga cha bungwelo pothandiza mabungwe enawo kuti naonso atukuke. M'menemu ndi m'mene ulilinso Mpingowa Nazarene. Iwo unapangidwa kudzasintha dziko lapansi pakufalitsa uthenga wa**Chiyeretso** cha m'mawu a Mulungu. Mpingowaukuluwu ndi umene unakhazikitsidwa kukhala wachiyeretso mu nthawi yomweyo. Utumuki wathu ndi kupanga ophunzira kukhala monga Khristu ku mafuko onse a dziko lapansi.

Moyo watsopano ndi tsogolo la Mpingo wa Nazarene wakhazikikapakutengapo mbali mu utumiki wa Mulungu. Choncho ndi chitsimikizo kuti ndi mpingowaYesu Khristu ndi bungwe limene linapangidwa mwapadera osangoti pa zimene limakhulupilira koma m'mene ukutengerapo gawo mwapadera pakukulitsa Ufumu wa Mulungu.

Pamene Mpingo waNazarene ukulowa mu zaka zina chikwi zatsopano (2000A.D), ndikoyenera kuzindikira zinthu izi zoonekeratu zapadera zimene tazivomereza ndikusangalala nazo mwachimwemwe. Chuma chathu chofunikira kwambiri ndi utumiki, maitanidwe, zikhulupiliro ndi zofunika zathu zapamwamba – tikuzipereka mokondwa ngati mphatso ku mibadwo imene ili nkudza.

Tikupemphera kuti zinthu zofunika zimeneife takhazikikamo kuti zidzapitirira kutumikira monga muuni wotsogolera kwa iwo amene akufunika kuyenda mkuwala ndi mu mthunzi wazaka zimene zili kutsogolo.

Zithu Zofunika Zomwe Takhazikikamo

1. Ndife Anthu Achikhristu

Monga Akhristu a mpingo woona, timagwirizana ndi okhulupilira onse pakudziwitsa anthu za Umbuye wa Yesu Khristu ndiko kuvomereza mfundo ya chikhulupiliro cha chikhristu ya Mulungu m'modzi mwa atatu. Timalemekedza kwambiri chiyero chimene chinayambitsidwa kalekale ndi a Wesley ndipo timakhulupilira kuti ndi njira yakumvetsetsa bwino chikhulupiliro chimene chili choona m'malembo, m'malingaliro, m'chikhalidwe ndi mkakhalidwe kake.

2. Ndife Anthu Achiyero

Mulungu amene ali woyera, akutiitana ife ku moyo umene uli wa chiyero. Timakhulupilira kuti Mzimu Woyera amafuna kuchita ntchito yachiwiri ya chisomo, imene imatchulidwa mu maunso ena monga 'kuyeretsedwa kwathunthu' ndi 'kubatizidwa ndi Mzimu Woyera' kutiyeretsa ife ku machimo onse: kutikonzanso mwatsopano m'chifanizo cha Mulungu: kutilimbikitsa ife kumkonda Mulungu ndi mtima wathu wonse, moyo wathu wonse, maganizo athu onse ndi mphamvu zathu zonse ndi anzathu onse monga m'mene ife tidzikondera ife eni.

3. Ndife Anthu Otumidwa

Ndife anthu otumidwa amene tavomera kuitana kwa Khristu ndi opatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera kupita m'dziko lapansi, ndikuchita umboni za Khristu Ambuye ndi kutengapo mbali ndi Mulungu pomanga mpingo ndi kukulitsa ufumu wake (2 Akorinto 6:1). Utumiki wathu: (a) Umayamba pakupembedzera; (b) Pakulalikira kwa anthu kudzera mukukopa anthu kuti abwere kwa Yesu ndiponso muzachifundo; (c) Pakulimbikitsa Okhulupilira kuti akhwime mu chikhrsitu kudzera m'maphunziro a ophunzira; (d) Pakukonzekeretsa amayi ndi abambo ku ntchito ya chikhristu kudzera mu maphunziro a pamwamba.

Kufotokoza Za Mitu Ili Pamwambayi

1. Ndife Anthu Achikhristu

Timagwirizana ndi okhulupilira onse pakudziwitsa anthu za Umbuye waYesu Khristu. Timakhulupilira kuti mu chikondi cha Mulungu, Mulungu amapereka kwa anthu onse chikhululukiro cha machimo ndi kubwezeretsansoubale wathu ndi Iye. Pakuyanjanitsidwanso ndiMulungu, timakhulupiliranso kuti tiyenera kuyanjanitsidwanso ndi wina aliyense, kukondana wina ndi mnzake monga m'mene Mulungu adatikondera, kukhululukirana wina ndi mnzake monga momwe Mulungu adatikhululukira.Timakhulupilira kuti moyo wathu pamodzi udzitsata chitsanzo chakakhalidwe ka Khristu.Taima pamodzi ndi Akhristu kulikonse pakutsimikiza mbiri ya mfundo ya Mulungu m'modzi mwa atatu yachikhulupiliro cha Akhristu, ndi mozamatimalemekeza khalidwe lachiyero chimene anatisiyira a Wesley kale.Timawerenga mawu a Mulungu (Buku Lopatulika) monga malo oyamba amene timapezamo zoona za uzimu kuti tipeze chitsimikizo ndi mfundo za chikhalidwe cha m'chitidwe wathu.

Ndi anthu onse a Mulungu timavomereza pakukweza Yesu Khristu Ambuye.

Yesu Khristu ndi Ambuye wa Mpingo, ndi monga m'mene chikhulupiliro cha atumwi chimatiuzira kuti, ndi m'modzi, woyera, wachilengedwe chonse ndi woperekamphamvu zonse. Mwa Yesu Khristu kudzera mwa Mzimu Woyera Mulungu amapereka chikhululukiro cha machimo ndi chiyanjano kudziko lonse.Amene amavomera chopereka cha Mulungu muchikhulupiliro amakhala anthu a Mulungu.
Pamene takhululukidwa ndi kuyanjanitsidwa mwa Khristu, timakhululuka ndi kuyanjana wina ndi mnzake. Mu njira imeneyi tili Mpingo wa Khrsitu ndi Thupi ndi kuulura umodzi wa Thupilo. Monga thupi limodzi, ubatizo umodzi. Timalimbikitsa mu umodzi wa mpingo wa Khristu ndipo timalimbika mu zinthu zonse kusunga izo (Aefeso 4:5, 3).

Yesu Khristu ndi Ambuye Woyera. Pa chifukwa ichi Mpingo wa Khristu sithupi limodzi lokha komanso ndi woyera. Ukufunika ukhale woyera ziwalo zake kwathunthu, woyera mwa Akhristu ake monga m'mene ulili mutu wake.Mpingo ndi woyera ndipo ukuitanidwa kuti ukhale woyera. Ndi woyera chifukwa ndi thupi la Khristu, amene wakhala kwa ife woonadi ndi wachiyero. Ukuitanidwa kukhala woyera ndi Mulungu, amene anatisankha asanaikidwe maziko a dzikolapansi kuti tikakhale oyera ndi opanda banga. Monga thupi limodzi la Khristu, moyowathu pamodzi monga mpingo tiimilire khalidweloyera la Khristu, amene anadzikhuthula yekha natenga maonekedwe a kapolo. Timavomereza chiyero cha Mpingo wa Khrsitu monga mphatso komanso maitanidwe.

Yesu Khristu ndi Ambuye wa mpingo. Pa chifukwa ichi, mpingo sithupi limodzi lokha koma kuti ndi woyera komanso wa onse kuphatikiza iwo amene amatsindikiza za zikhulupiliro zofunika za chikhulupiliro cha chikhristu. Timatsimikiza za chikhulupiliro chotitimalandira mphamvu kuchokera kwaMulungu chimene chili mwa Akhrsitu kulikonse ndi munthawi zonse. Timavowereza izi pa mfundo ya Wesley yoti 'tonse ndi mzimu umodzi' umene umatithandiza kukhala pa umodzi ndi amene amagwiritsa ntchito mawu a Mulungu kukhala ofunikira ndipo timalolerana ndi amene samagwirizana ndi ifepankhani zimenezili zosafunikira pa chipulumutso.

Yesu Khristu ndi Mbuye wa mawu a m'Buku Lopatulika. Pachifukwa ichi mpingo sithupi limodzi lokha, woyera ndi wa onse komanso ndi wochokera kwa Iye amene amapereka mphamvu zonse. Unamangidwa ndi madziko a atumwi ndi aneneri ndipo mopitiriza umadzipereka ku zophunzitsa za atumwi. Mpingo umayang'ana makamaka pa mawu a m'Bulu Lopatulika, amene ali chinthu chokhacho cha chikhulupiliro ndi moyo wake. M'mene mawu a Mulungu amafotokozera za Umbuye wa Yesu Khristu zimatanthauza kuti timamvetsetsa Mawu a Mulungu kudzera mwa Mzimu Woyera amene amachitira umboni za Iye. Pakutsindika ndi kukonza mamvekedwe athu a Mawu a Mulungu timapereka ulemu ndi kukumbikira zikhulupilirro zakale ndi Akhristu ena amene analankhulapo ndikufotokoza mokhulupirika mawu a Mulungu. Timalolanso kumvetsa kwathu kwamawu a Mulungu kuti kutsogozedwe ndi mawu a Mzimu Woyera amene

amatilankhula mkulapa, mchikhulupiliro ndi muchitsimikizo. Pomaliza timayesa kumvetsa kwathu mawu a Mulungu pakufuna kamvetsedwe kake koyenera ndi kugwirizana kwake pa umboni wa kwa Yesu Khristu.

Tinaitanidwa makamaka kukachitira umboni za chiyeretso cha mpingo wa Khristu m'mene timavomerezera a Wesley pa za chiyero. Timatsimikiza mfundo za chipulumutso ndi chisomo chokha kudzera m'chikhulupiliro mwa Yesu Khristu Mpulumutsi wathu. Pakutero timapitiriza kutsimikiza kuti mpingo wa Khristu ndi umodzi wa onse ndi woyang'anidwa ndi Iye. Koma maitanidwe athu apadera ndi kuonetsa pamaso pa dziko lonse ndi mpingo kuvomerezedwa kwa chiyero kuchokera ku mbali zonse ndi kulimbikitsa anthu a Mulungu kukhala m'chikondi chodzala cha Atate woyera. Pachifukwa ichi timatsimikiza za kamvetsedwe ka Wesley pa nkhani ya chiyero ndipo timafuna kukhala okhulupirika mu ziphunzitso zake zazikulu zomwe ndi: Chisomo cha Mulungu chimene chimagwera anthu asanatembenuke ndi njira za chisomo, kulapa, chikhulupiliro, kubadwanso mwatsopano, kuchotsedwa kwa machimo, chitsimikizo, gulu la Akhristu ndi khalidwe lake ndi chikondi chopanda banga.

2. Ndife Anthu A Chiyero

Tinaitanidwa ndi mawu a Mulungu ndi kukokedwa ndi chisomo kumpembedza Mulungu ndikumukonda Iye ndi mtima wathu wonse, moyo wathu wonse, maganizo athu onse ndi mphamvu zathu zonse ndi anzathu monga m'mene tidzikondera eni. Kumapeto ake timadzipereka kotheratu kwa Mulungu, pakukhulupilira kuti tingapatulidwe kwathunthu kachiwiri monga m'mene tinalili poyamba. Timakhulupilira kuti Mzimu Woyera amadzudzula, pamene chisomo cha Mulungu chikutisintha tsiku ndi tsiku mkukhala anthu a chikondi ndi khalidwe la uzimu, m'moyo ndi thupi, ndi achifundo ndi a chilungamo. Ndi ntchito ya Mzimu Woyera imene imatibweretsa mu chifanizo cha Mulungu ndichiyero m'moyo wa anthu okhulupilira chimamvetsedwa bwino monga m'mene alili Khristu.

Timakhulupilira Mulungu Atate, Mlengi, amene amakhalitsa moyo zinthu zomwe kulibe, poyambilira ife kunalibe, koma Mulungu

anatiitana ife kukhala anthu, natipanga mwa Iye yekha, ndipo natikhalitsa muchifanizo chake. Tatumidwa kunyamula chifanizo chaMulungu."*Pakuti Inendine Yehova Mulungu wanu; potero dzipatuleni, ndipo mudzikhala oyera; pakuti Ine ndine Woyera*" (Levitiko 11:44)

Njala yathu yakukhala anthu a chiyero ikuchokera mu chiyero cha Mulungu mwini. Chiyero cha Mulungu chimakamba za Umulungu wake komanso chikhalidwe chake mwa Iye yekha. Palibe wofanana ndi Iye mu Ufumu ndi mu Ulemerero. Kuyankha koyanera kwa munthu mu ulemerero wotere ndi kumpembedza Mulungu monga Mulungu. Chiyero cha Mulungu chimaoneka mu ntchito yake ya chiombolo chathu.Pakukumana ndi Mulungu amene amadziulula yekha ndikudzipereka yekha amapangitsa kupembedza kukhala kotheka, ndipo kupembedza kumakhala njira yoyambilira yomudziwira Iye.Timapembedza Mulungu woyera ndi wotiombola pakukonda zomwe Iye amakonda.

Kapembedzedwe kathu ka Mulungu wachisomo wamkuluyi kamakhala m'njira zosiyanasiyana.Nthawizambiri ndikumtamanda ndi pemphero la anthu a chikhulupiliro. Kapembedzedwe kameneka kamaonekanso mu zochita zathu m'mapemphero a mseri, pakupereka zopereka ndi kumtamanda ndi kumvera, utumiki wathu wogawana chikhulupiliro, chifundo kwa anzathu, kufuna chilungamo ndi machitidwe athu owongoka ndi mchitidwe wa kapembedzedwe pamaso pa Mulungu woyera ndi chiyero. Angakhale ntchito zathu za moyo uno zimakhala kachitidwe kathu kakupembedza ndipo zimakhala zofunikira kwambiri mu uzimu pamene kupembedza Mulungu Woyera kumakhalamoyo wosatha.

Yesu Khristu anaulura Mulungu m'modzi woyera ndipo anakhala chitsanzo pakupembeza mkukhala wa chiyero kwa ife. Yesu amatidziwitsa kumvetsa kwathu kwa chiyerokudzera m'moyo wake, kudzipereka nsembe kwake ndi mu zophunzitsa zake monga m'mene zimapezekera m'mabuku a uthenga wabwino makamaka chiphunzitso cha pa phiri. Monga anthu a chiyero timafuna tidzikhala monga Yesu m'malingaliro ndi m'machitidwe athu. Mwachisomo chake Mulungu amathandiza okhulupilira amene

amampembedza ndi mitima yawo yonse kukhala monga Yesu. Ichitimachitenga kukhala chofinikira cha chiyeretso.

Mulungu watipatsanso ife mphatso ndi mtolo wakusankha. Chifukwa choti tinabadwa ndi tchimo timasakha njira zathu m'malo mwa njira ya Mulungu (Yesaya 53:6).Pakudetsa chilengedwe cha Mulungu ndi tchimo, ndife akufa ndi zolakwa ndi zochimwa zathu (Aefeso 2:1). Ngati tingakhalenso m'moyo wa uzimu, Mulungu amene amakhalitsa zinthu zosakhala ayenera kutilenganso mwatsopano kudzera mu chiwombolo cha Mwana Wake.

Timakhulupilira kuti Mulungu analowa m'dziko lapansimukusandulika thupi mwa mwana wake, Yesu Khristu waku Nazarete, Mulungu Munthu wotchuka. Yesu anabwera kudzakonzanso chifanizo cha Mulungu mwa ife, kutithandiza kuti tikhale anthu oyera. Timakhulupilira kuti chiyero m'moyo wa munthu wokhulupilira ndi chovuta ndipo chimatenga nthawi ya moyo wa munthu. Pamene taphukanso, mzimu wa Ambuye wathu amatikoka mwachisomo kuchipatuko chathunthu ndi cha moyo wathu ndi Iye kenako mukuyeretsedwa kwathu kwathunthu amatichotsa ku uchimo weniweni nakhala mwa ife - Mzimu wake amatikonza ife muchikondi chopanda banga mkutithandiza kukhala m'moyo woongoka kutipatsa mphamvu kuti titumikire.

Mzimu wa Yesu umagwira ntchito pakati pathu kuturutsa zipatso zachikondi monga zomwe zinali mwa Iye za chikondi choyera. Ndipo Iye amatithandiza ife '*Nimubvale munthu watsopano, amene analengedwa monga mwa Mulungu, m'chilungamo, ndi m'chiyero cha choonadi'* (Aefeso 4: 24). Kukhala monga Mulungu ndiko kukhala monga Yesu.Pamene maokedwe a uzimu a chifanizo cha Mulungu abwezeretsedwa kwa ife mu m'chitidwe wa kuyeretsedwa kwathunthu, timavomereza kuti sitinafikepo m'moyo wathu wa uzimu; cholinga chathu cha moyo uno ndikukhala monga Yesu m'maganizo ndi muzochita zathu. Pakupitiriza kulolera, kumvera ndi chikhulupiliro "Tisandulika m'chithunzithunzi chomwechi kuchokera ku ulemerero kunka ku ulemerero monga ngati kuchokera kwa Ambuye wathu" (2 Akorinto 3:18). Timatengaponso gawo popitilira pamenepa tikhalamoyo wopembedza umene umaonetsedwa m'njira zambiri kuphatikizapo kuvomereza maitanidwe a uzimu ndi pakusonkhana pamodzi molingana ndi m'mene mpingo umafunira. Monga thupi la okhulupilira amene

timapembedza limodzi, timayesetsa kukhala amodzi monga Khristu, pakupembedza Mulungu ndi mtima wathu wonse ndi kulandira mphatso zake za chikondi, zakuyeretsa, zamphamvu ndi za chifundo.

Monga anthu a chiyero, sitimapezeka mumpata umene umapezeka mu mbiri yakale ndi ya chipembedzo.Timadziwika ndi Chipangano Chatsopano ndi Mpingo woyamba.Mfundo zathu zotsatira za chikhulupiliro zimatiika pamalo odziwikiratu kuti ndife Akhristu ovomerezeka ndi odziwika. Timadziwika ndi chikhalidwe cha chisomo cha ulere (Yesu adafera onse) ndi ufulu wa anthu – ndi mulingo umene Mulungu anatipatsa wakusankha Mulungu ndi chipulumutso. Timatsatiranso mbiri yathu ya chipembedzo kuchokera kwa a Wesley mu zaka za m'ma 1700 A.D. ndi ku gulu la chiyero la mu zaka za m'ma 1800 ndi 1900 AD.

Mu zaka zikwizikwi anthu a chiyero atengeka kwakukulu ndi Yesu. Timapembedza Yesu: timakonda Yesu! Timaganiza za Yesu! Timakamba za Yesu! Timakhala ndi Yesu! Ichi ndicho chiyambi chathu chofunikira ndi kusefukira kwa chiyero pa ife. Izi ndi zimene zimafotokoza za khalidwe la anthu a chiyero.

3 Ndife Anthu Otumidwa

3a. *Utumiki Wathu Wakupembedza*

Utumiki wa mpingo ku dziko lino lapansi umayamba pakupembedza. Ndi m'mene monga timakomanirana pamodzi pamaso pa Mulungu pakupembedza – kumuyimbira, kumva kuwerenga kwaMawu a Mulungu, kupereka chakhumi chathu ndi zopereka, kupemphera. Kumva Mawu a Mulungu amene alalikidwa, kubatizidwa ndi kudya Mgonero wa Ambuye – zimenezi zimatidziwitsa bwinobwino kuti zimatanthauza chiyani kukhala anthu a Mulungu. Chikhulupiliro chathu choti ntchito ya Mulungu m'dziko lapansi imakwaniritsdidwa poyambilira kudzera mu anthu amene akupembedza pamodzi mtchalitchi chimatitsogolera kumvetsa bwino kuti utumiki wathu timaphatikizanso: kulandira Akhristu atsopano mu mpingomo komanso kudzala mipingo ina yatsopano.

Kupembedza ndi chinthu chofunikira kwambiri chimene chimaonetsera chikondi chathu kwa Mulungu. Timapembedza ndi kukweza monyadira Mulungu yekhayo ndi kumpatsa ulemu amene mu chisomo ndi chifundo anatiombola ife. Chiyambi chenicheni chakupembedza ndi pampingo pamene anthu a Mulungu amakomana, osakhala mu zofuna zawo kapena pakudzipatsa ulemerero wokha, koma pakugonja ndi kudzipereka kwawo, kupembedza ndi mpingo mukukonda ndi kumvera kwa Mulungu.

Kupembedza ndi mwayi wapadera woyamba komanso ndi udindo wa anthu a Mulungu. Ndi kukumana kwa anthu a chipangano pamanso pa Mulungu pakubukitsa ndi kukondwera pachifukwa chimene Iye ali, pa zimene Iye wachita, ndi zimene adalonjeza kudzachita. Mpingo m'kupembedza uli pa ngodya yofotokoza kapena kudziwitsa ena za ife. Mpingo wa Nazarene umakhulupilira kupembedza pampingo ndipo umu ndi kudzera mwa anthu opembedzawa m'mene utumiki wathu umakwanitsidwa. Utumiki wa mpingo umapeza tanthauzo lake ndi zolinga zake mkupembedza, kulalikidwa kwa mawu, kukondwelera za imfa ya Ambuye, kuwerengedwa kwa mawu mtchalitchi, kuyimba nyimbo ndi makolasi, pemphero lomangirira zonse ndi kupereka chakhumi ndiponso zopereka zimene zimatidziwitsa kuti zimatanthauza chiyani kukhala anthu a Mulungu. Kudzerapakupembedza m'mene timamvetsetsa bwino bwino kuti kodi zimatanthauza chiyani pakutengapo gawo ndi Mulungu mu ntchito ya chiombolo.

Utumiki wathu wakupembedza ndi madziko a mpingo wathu. Monga Mpingo wa Nazarene umakhulupilira kupembedza pa mpingo kuti ndikofunika, kudzipereka kwathu kopitiriza pakuyambitsa mipingo ina yatsopano.

3b. *Utumiki Wathu Wa Za Chifundo Ndi Wokopa Anthu Kubwera Kwa Yesu*

Monga ife anthu amene tapatuliwa kwa Mulungu, timagawana naye chikodi chake cha pa otayika za chifundo zake kwa osauka ndi osweka mtima. Lamulo lalikulu ndi udindo waukulu umatisuntha ife ndikutipangitsa kuyamba kudziko lapansi utumiki wokopa anthu kuti abwere kwa Mulungu, utumiki wa chifundo ndi wa chilungamo. Kumapeto ake tili odzipereka kuitana anthu ku chikhulupiliro, kusamalira iwo amene ali osowa, pakuletsa chisalungamo ndi kuteteza oponderezedwa, kugwira ntchito poteteza ndi kusunga chilengedwe cha Mulungu, ndi kuphatikiza ena onse amene aitana padzina la Ambuye.

Kupyolera mu utumiki umenewu kudziko, mpingo umaonetsa chikondi cha Mulungu.Nkhani ya Buku Lopatulika ndi nkhani yokamba za Mulungu pamene akuyanjanitsa dziko lapansi kwa Iye, mwakufunikira kwake kudzera mwa Yesu Khristu (2 Akorinto 5:16-21). Mpingo watumidwa ku dziko kukatengapo gawo pamodzi ndi Mulungu mu utumikiwachikondi ndi wa chiyanjano kudzera mu utumiki wokopa anthu, utumiki wa za chifundo ndi za chilungamo.

Udindo wathu waukulu ndi lamulo lalikulu, zonse zili zofunika pakumvetsa kwathu kwa utumiki wathu. Pali ziganizo ziwiri za utumiki umodzi, mbali ziwiri za Uthenga Wabwino. Yesu amene amatitsogolera ku lamulo ili: "Udzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wonse, ndi moyo wako wonse ndi nzeru zako zonse… ndipo udzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini" (Mateyu 22:31) akutiuzanso kuti, "Chifukwa chake mukani, phunzitsani anthu amitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu" (Mateyu 28:19-20).

Ntchito ya mpingo kudziko lapansi imafika ku mtundu wonse wa anthu, monga anthu, olengedwa mchifanizo cha Mulungu, tili ofunikira ndithu ndi ntchito yathu kukonda ndikuwatenga anthu monga m'mene alili monga momwe Mulungu awakondera ndi kutengedwa pamaso pake, amene amawasakira mtendere, chilungamo ndi chipulumutso kuchokera ku uchimo kudzera mwa

Khristu. Ndi ntchito yathu kukhala ndi chifundo ndi kusamalira iwo osowa. Ndi ntchito yathu kuletsa zinthu za dziko lapansi ndi mfundo zake zimene zimamutchipitsa munthu mtengo kapena kumulanda mphamvu.

Ntchito ya mpingo imafikira kwa munthu aliyense. Mulungu watilenga ife kukhala anthu athunthu, ndipo ndi ntchito yathu kuti tikakhale atumiki ake a chikondi cha Mulungu kwa anthu onse, - thupi lonse moyo wonse, ndi mzimu wonse. Utumiki wathu wakukopa anthu, wa zachifundo ndi chilungamo ndi ntchito imodzi yosakanikirana, kuwatumikira anthu muthupi,kuthupi ndi muzosowa zawo za uzimu.

Ntchito yampingo kudziko ikufikira mtundu wa anthu onse chifukwa cha Yesu Khristu amene wabwera m'dziko kupulumutsa onse oitana pa dzina lake. Monga anthu a Mulungu ndi mwayi wathu wapadera ndi mtolo wathu kugawana Uthenga Wabwino ndi onse akumva, kaya ndi mtchalitchi, kaya paiwe wekha pakuchitira umboni " chokhumba chathu ndikugwiritsa ntchito mwayi uliwonse pakuitana anthu ku chikhulupiliro mwa Yesu Khristu."

Ntchito ya mpingo ikufikira kwa anthu onse chifukwa cha Mzimu Woyera, amene pa Pentekoste anakhuthulidwa kwa anthu onse (Machitidwe 2). Ndi ntchito yathu kudziwitsa munthu aliyense Uthenga Wabwino wa chipulumutso kudziko lino. Talimbikitsidwa ndi Mzimu Woyera kupita kudziko lonse ndi kukalalikira za Ufumu ndi kutengapo gawo ndi Mulungu pakumanga mpingo.

Ndi chifukwa cha mzimu wathu wa chiyembekedzo ndi wa chikhulupiliro kuti zonse zitheka ndi Mzimu amene watipangitsa kukagwira ntchito imene tinapatsidwa ndi Mulungu. Ndi mzimu amene amaposa kudziwa kwa munthu kapena Khama lake. Utumiki wathu ndiko kuyankha kuitana kwa Mulungu. Ndikutengapo gawo ndi Mulungu mu ufumu mu utumiki wa kuyanjanitsa. Ndi mboni yokhulupirika ya mpingo ndi chisonyezo cha chikondi cha Mulungu ku dziko – utumiki wokopa anthu, za chifundo ndi chilungamo. Ndi chikhulupiliro chathu pa luntha la chisomo cha Mulungu kusintha

miyoyo ya anthu yoonongeka ndi machimo ndi kuwabwezeretsanso muchifanizo chake.

3c. Utumiki Wathu Pakukhala Ophunzira

Ndife odzipereka kwa anthu – ndikuitana ena kukhala – ophunzira a Yesu. Pokumbukira ichi ndife odzipereka kupereka njira (Sande sukulu, maphunziro osanthula Buku Lopatulika, magulu ena aulangizi ndi zambiri zina kudzera m'mene okhulupilira amalimbikitsidwa mkukula mu mamvetsedwe awo). Chikhulupiliro chachikhristu ndi ubwenzi wa wina ndi mnzake ndi Mulungu. (Timadziwa kuti kukhala wophunzira timaphatikizapo kudzipereka tokha pakumumvera Mulungu ndi kutenga chikhalidwe cha chikhristu.Timakhulupilira kuti tiyenera kuthandizana wina ndi mnzake kukhala m'moyo woyera kudzera mukuthandizana kwathunthu, pakusonkhana pamodzi Akhristu ndi udindo wakukondana. Wesley anati,"Mulungu watipatsa ife kwa wina ndi mnzake kuti tilimbikitsane wina ndi mnzake."

Kukhala wophunzira wa Khristu ndi chikhalidwe cha moyo. Ndi njira yophunzilira m'mene Mulungu amafunira kuti tidzikhala m'dziko. Pamene tiphunzira kukhala omvera mawu a Mulungu, pakuvomereza chikhalidwe cha chikhulupiliro, ndikukhala waudindo pa wina ndi mnzake, timayamba kumvetsa chimwemwe chenicheni cha moyo wakhalidwe labwino ndi tanthauzo la chikhristu la ufulu, kukhala wophunzira sikhama la munthu yekha, ndikuvomereza malamulo ndi ndondomeko. Ndi njira imene Mzimu Woyera amatibweretsa pang'onopang'ono mukukhwima mwa Khristu.Ndikudzera mu wakuphunzira m'mene timakhala a khalidwe la chikhristu.Mapeto ake a cholinga cha kukhala wakuphunzira ndi kusinthidwa kuti tikhale monga Yesu Khristu (2 Akorinto 3:18).

Pakuwerenga ndi kulingalira mozama pa Mawu a Mulungu, Akhristu amapeza akasupe opumulira mu chigwa chilichonse cha ludzu pa ulendowawo wakukhala ophunzira.Pakupangidwa mwatsopano pa kutsukidwa kwa mawu, pakukonzedwanso pakukhala m'mawu,

pakumva mozama zoona za mawu, akuphunzira amadzapeza chikondwerero chodabwitsa kuti "… *Mwakukonzanso kwa mtima wanu*…" (Aroma 12:2). Njira ya chikhristu imatseguka patsogolo pawo ngati msewu waukulu wotsegula. Motsogozedwa ndi Mulungu, amadutsa m'njira ya moyo imene imaonetsa zochita ndi chikhalidwe cha munthu. Pakukonzedwanso ndi kasupe wa mawu, ophunzira amapereka miyoyo yawo modzipereka kupitirira muyezo pawokha mu ntchito yawo.

Timatsindika za moyo woperekedwa wa mtengo wake khalidwe la uzimu umene aliyense atha kuuona bwino pakuphunzitsa amayi ndi abambo kukhala ophunzira aYesu. Khalidwe la pemphero ndi kusala kudya, kupembedza, kuphunzira, kupeza nthawi yawekha yabwino, kudzipereka mofuna pa nthawi imodzi m'moyo wa okhulupilira.

Kukhala ophunzira kumafuna kudzipereka kuchokera ku mbali zonse ndi kukhala m'dziko mwa chikondano. Mwa ife tokha, ochepa mwa ife tithe kuyambitsa khalidwe la uzimu limene lingatipangitse kukula mu uzimu. Timakhulupilirakuti tiyenera kulimbikitsa njira zomwe zaikidwa mbali zonse monga: Sande sukulu, magulu a ophunzira, kuphunzira Buku Lopatulika, mapemphero ndi chilangizo cha chikhristu chimene chili chofunikira kupanga moyo wathu wa uzimu ndi kuukhwimitsa. Pakuzindikira ntchito ya mdindo ya a Wesley m'misonkhano yawo imatilimbikitsa ife kuyivomereza m'mapembedzedwe athu a chikhristu.

3d. Utumiki Wathu wa Maphunziro A Pamwamba

Tili odzipereka ku maphunziro a chikhristu, m'meme kudzera m'menemo timakonzekeretsa abambo ndi amayi ku utumiki wa chikhristu kudzera m'maseminale athu, m'makoleji ndi m'masukulu ena apamwamba, tili odzipereka pakufuna nzeru, kupanga khalidwe la chikhristu ndi kukonzekeretsa atsogoleri kuti tikwaniritse maitanidwe athu opatsidwa ndi Mulungu otumikira mu mpingo ndi kudziko lapansi.

Maphunziro a pamwamba a chikhristu ndi mbali yofunikira ya utumiki ya Nazarene. Mu zaka zoyambilira za Mpingo wa Nazarene masukulu athu apamwamba amagwiritsidwa ntchito ndi cholinga chokonza abambo ndi amayi a Mulungu ku utsogoleri ndi utumiki wa chikhristu kudziko lonse kuti afalitse za chiyero chomwe a Wesley adaphunzitsa. Kupiriza modzipereka kwathu m'maphunziro a pamwamba a chikhristu kwatulutsa dziko lonse maseminale, sukulu za ubusa, makoleji ndiponso sukulu za yunivesite.

Utumiki wathu wa maphunziro a pamwamba umachokera pamene tidziwa tanthauzo lakukhala anthu a Mulungu. Tiyenera kumukonda Mulungu ndi 'Mtima wathu wonse, moyo wa wonse ndi maganizo athu onse.' Choncho tiyenera kukhala adindo abwino pakukulitsa nzeru zathu, maphunziro athu, ndi pakugwiritsa ntchito nzeru zathu mwa ichi tili odzipereka moonekera ndi moona pakufunabe nzeru ndi chilungamo mogwirizana ndi chikhulupiliro chathu chimodzi cha chikhristu. Maphunziro a pamwamba a Akhristu ndi bwalo lofunikira lochulukitsira nzeru zathu pakukhala adindo, komanso ndi bwalo limenelapangidwa ndi cholinga chomwe chadziwidwa ndi kukambirana ndi kupeza zoonadi ndi kudziwa za Mulungu ndi chilengedwe chonse cha Mulungu.

M'maphunziro apamwamba a chikhristu, chikhulupiliro sichimayikidwa magulu ena, koma chimaphatikizidwa modabwitsa pamodzi ndi zophunzirazo monga m'chikhulupiliro ndi maphunziro. Munthu aliyense amapangidwa m'dera lililonse la maganizo ndi moyo wake mogwirizana ndi zokhumba ndiponso zopanga za Mulungu. Mchitidwe wachikhristu ndi kukonzekeretsa atsogoleri ku utumiki wa mu mpingo ndidziko umapangidwa kuchokera mu gawo la kuphunzira za Mulungu, pa maphunziro a pamwamba achikhristu pakupanga munthu wathunthu ndikofunikira pakupanga abambo ndi amayi achikhristu mu utumiki wa utsogoleri mu mpingo ndi dziko.

Monga anthu owomboledwa oitanidwa kukhala monga Khristu ndi wotumidwa monga atumiki a chikondi cha Mulungu, timatengapo mbali pamodzi ndi Mulungu mu ntchito yoombola mtundu wa anthu.

Maphunziro achikhristu apamwamba amathandiza kwambiri mu umunthu wathu monga anthu otumidwa – pakupereka nzeru zochuluka ndipo ndi wofunikiranso pakutumikira Mulungu bwino m'masukulu athu. Kukhulupirika kwathu pakutengapo mbali mu ntchito ya chiwombolo ya Mulungu amene atha kukhala atsogoleri antchito a Khristu mu mpingo komanso m'dziko lapansi.

Dziko lapansi limene tayitanidwa kukatumikiramo likukhala lolumikiza pafupifupi ndi losintha mosokonezeka tsiku lililonse. Pamene ntchito ya Mulungu ya chiwombolo ikupitirira chitsogolo m'mibadwo ino ndi m'mibadwo ya mtsogolo, umboni wathu wokhulupirka ku za Umbuye wa Khrsitu ndi kutengapo mbali ndi Mulungu pakumanga mpingo bwino lomwe udzapitiriza kufuna kudzipereka kwathunthu ku maphunziro apamwamba a Khristu.

NDEMANGA

Pamene timayamba zaka za m'ma 1900A.D. Mpingo wa Nazarene unabadwa: P.F. Bresee ndi ena anali otsimikizidwa kuchokera mkati kuti Mulungu waitana iwo kufotokoza cholinga chouza mpingo ndi dziko lapansi m'njira imene a Wesley amenenso adakamba za chiyero anachitola! Pakuti ndikuchita kokhako kwa mphamvu ya Mulungu mu nthambi ya chipembedzo imeneyi kumene kukuonekera kuchokera ku gulu lomwe linalibe luntha lina lililonse, Mpingo wa Nazarene tsopano uli ndi anthu oposa 1.3 million owatsatira ndipo ukutumikira m'maiko 119 ku dziko lapansi.

Pamene timaymba zaka za m'ma 2000 A.D. tsogolo la chipembedzo chimenechi lidaoneka lowala kuposa kale: ambiri akukhulupilira kuti tinakhazikitsidwa kuti titumikire mu zaka za m'ma 2000 A.D. osati muzaka za m'ma 1900 A.D. tayikidwa pamalo omwe tikufuna kutenga nawo mbali yaikulu mu dziko ili lamakono. Chitsimikizo chimenechi chapezeka mu ziphunzitso za chiyero za a Wesley ndi mfundo yake yofunikira ya chisomo chosakayikitsa. Tikhulupilira kuti mtundu wa anthu utha kusintha tsopano lino kukhala wofunikira ndi wokhazikika wosinthidwa ndi chisomo cha Mulungu. Tili ndi chitsimikizo chosatheka kuchigonjetsa mu uthenga uwu wa chiyembekedzo, chimene chichokera kumtima wa Mulungu woyera.

P.F. Bresee amakonda kunena kuti “Dzuwa siliwala m’mawa.” Ndi m’mawabe wa Mpingo wa Nazarene ndipo dzuwa silingalowe muchipembedzo chathu kudziko lapansi. Tili ndi chiyembedzo chokhazikika chofunika pakufuna kusuntha dziko lapansi ndi uthenga wathu wa ‘chiyero’ mu zaka zino za m’ma 2000 A.D. ndi masomphenya owonekeratu, kudzipereka kwathunthu ndi chikhulupiliro chosasunthika, tikuona zaka izi za m’ma 2000 ngati mwayi wathu wopanga ophunzira kukhala onga Khristu anthu a mitundu yonse.

***

Christian Holiness Missional
Chichewa

First Printing – 1000 – July 2004

ISBN 0-7977- 0673-9

Translated and printed with permission by

Africa Nazarene Publications

P.O. Box 1288

Florida

1710

Republic of South Africa

Africa NazarenePublications

Core Values - Chichewa